ndi imfa yosatha?
-Kodi mukudziŵa kuti Mulungu Mpulumutsi yekha ndi amene angathe kukupulumutsani inu?

-Ngati mukudziŵa zimenezi, Yesu anati anabwera pa dziko la pansi pano kuti akhale Mpulumutsi wanu.



PHUNZIRO LA 52

1. Kodi Nikodemasi anadziŵa bwanji kuti Mulungu ndi amene anamutumiza Yesu?
-Chifukwa chakuti Yesu ankachita zozizwitsa zambiri zimene zingachitidwe ndi Mulungu yekha.

2. Kodi "kubadwanso mwa madzi" kukutanthawuza "kubatizidwa?"
-Iyayi.

3. Kodi Yesu ankatanthawuza kuti tiyenera kubatizidwa kuti tibadwenso kaŵiri?
-Iyayi.

4. Kodi kubatizidwa kungatipulumutse ife?
-Iyayi.

5. Kodi nanga Yesu ankatanthawuza chiyani ndi mawu akuti "kubadwanso mwa madzi?"
-Kubadwanso mwa madzi kukutanthawuza kuti tiyenera kulapa machimo athu kuti Mulungu atiyeretse ku machimo athuwo.

6. Kodi nanga Yesu ankatanthawuza chiyani ndi mawu akuti "kubadwa mwa Mzimu."
-Kubadwanso mwa Mzimu kukutanthawuza kuti Mulungu Mzimu Woyera ayenera kupereka moyo watsopano kwa mzimu wathu.

7. Kodi Yesu ankatanthawuza chiyani ndi mawu akuti, "Mnofu umabereka mnofu, koma Mzimu umabereka Mzimu?"
-Yesu ankatanthawuza kuti mnofu ungathe kubereka mnofu okha, ndipo Mulungu Mzimu Woyera ndi amene angathe kubereka mzimu wa munthu.

8. Kwa Mulungu, pali anthu a mitundu yiŵiri yokha pa dziko la pansi. Kodi mitundu imeneyi ndi yiti?
-Anthu amene anabadwa kamodzi ndi anthu amene abadwanso kachiŵiri.

9-Kodi anthu amene abadwanso kachiŵiri ali m'banja la ndani?
-Banja la Mulungu.

10. Kodi Yesu akufanana bwanji ndi njoka ya mkuwa imene Mulungu anamulamula Mose kuti apange m'chipululu muja?
-Apa pali zimene analankhula Yesu:
-Yesu adzapachikidwa ngati m'mene njoka ya mkuwa inapachikidwira pa mtengo.
-Yesu adzaŵapulumutsa anthu amene akumukhulupilira Iye ngati m'mene anapulumutsidwira a Isirayeli amene anayang'ana pa njoka ya mkuwa ija.

11. Kodi chifukwa chiyani Mulungu anamutumiza Yesu pa dziko la pansi pano?
-Mulungu anamutumiza Yesu kudzaŵapulumutsa anthu ku mphamvu ya tchimo.
-Mulungu anamutumiza Yesu kudzaŵapulumutsa anthu ku mphamvu ya imfa.
-Mulungu anamutumiza Yesu kudzaŵapulumutsa anthu ku mphamvu ya Satana.

12. Kodi anthu okhulupilira mwa Yesu adzaŵeruzidwa ndi Mulungu?
-Iyayi.

13. Kodi chifukwa chiyani anthu amene sakukhulupilira mwa Yesu aŵeruzidwa kale ndi Mulungu?
-Chifukwa chakuti anthuwo sakukhulupilira kuti Yesu ndi



17-Ndipo Yesu atamva izi, anati kwa iwo, "Sali anthu angwiro amene amafuna sing'anga, koma odwala. Sindinabwelere kudzaŵayitana olungama koma ochimwa."

-Yesu anaŵawuza Afarisi kuti anthu angwiro safuma sing'anga, koma odwala.

-Kodi Yesu ankatanthawuza chiyani?
-Yesu ankatanthawuza kuti sanabwere kudzaŵapulumutsa anthu amene sakudziŵa kuti iwo akudwala.
-Yesu anadza kudzaŵapulumutsa iwo amene akudziŵa kuti akudwala.

-Apa pali chitsanzo:

-Kodi ngati munthu akudwala koma sakudziŵa, angathe kupita kwa sing'anga?
-Iyayi.

-Kodi chifukwa chiyani?
-Chifukwa chakuti sakudziŵa kuti akudwala.

-Yesu sanabwere kudzaŵapulumutsa anthu amene akukhulupilira kuti ndi opanda tchimo.

-Yesu anabwera kudzaŵapulumutsa anthu amene akudziŵa kuti amuchimwira Mulungu, ndipo Mulungu yekha ndi amene angathe kuŵapulumutsa iwo.

-Kodi nanga inu?

-Kodi mukudziŵa kuti munabadwira mu tchimo?
-Kodi mukudziŵa kuti mwamuchimwira Mulungu?

-Kodi mukudziŵa kuti Mulungu amalanga machimo onse

M’bayibulo.

-Chifukwa chakuti Levi anali okondwa pokhulupilira mwa Yesu ngati Mpulumutsi wache, Levi anamuyitanila ku nyumba kwache Yesu ndi amuna ena kuti akadye naye.

Tiyeni tiŵerenge Maliko 2:15-16

15-Pamene Yesu ankadya mgonelo ku nyumba kwa Levi, anthu ambiri okhometsa msonkho ndi “ochimwa” ankadya naye pamodzi ndi ophunzira ache, chifukwa chakuti anatsatiridwa ndi anthu ambiri.

16-Pamene aphunzitsi a malamulo amene anali Afarisi, anamuwona akudya ndi anthu “ochimwa” ndi okhometsa msonkho, anaŵafunsa ophunzira a Yesu kuti: “Kodi chifukwa chiyani Yesu akudya ndi okhometsa msonkho ndi “ochimwa”

-Kodi aphunzitsi a malamulo amene anali Afarisi anati chiyani atamuwona Yesu akudya ndi Levi ndi anthu ena?
-Anati kuti, Kodi chifukwa chiyani Yesu akudya ndi anthu okhometsa msonkho ndi ochimwa?”

-Afarisi sankakhulupilira kuti iwo anali ochimwa.
-Afarisi ankakhulupilira kuti anali opanda machimo.

-Afarisi sankamvetsetsa zakuti anthu onse anabadwira mu uchimo.

-Afarisi sankamvetsetsa zakuti anthu onse amuchimwira Mulungu.

-Kodi Yesu analankhula chiyani atamva zimene ankalankhula Afarisi?

Tiyeni tiŵerenge Maliko 2:17



Mulungu Mpulumutsi.

14. Kodi chifukwa chiyani anthu sakufuna kuŵamvera mawu a Mulungu?
-Chifukwa chakuti anthuwo akuŵakonda machimo awo.

-Tsiku lina lache, Yesu anabwelera ku mudzi wa Kapenamu.

Tiyeni tiŵerenge Maliko 2:1-2

1-Patapita masiku angapo, Yesu atalowânso mu Kapenamu, anthu anamva kuti ali m’nyumba.

2-Chomcho anthu ambiri anasonkhana kotero kuti mpaka anasoŵa malo mpaka panja pa khomo, ndipo analalikira mawu kwa iwo.

-Anthu ambiri ankabwera kudzamumvera Yesu akuphunzitsa.
-Yesu ankaŵaphunzitsa iwowo Mawu a Mulungu.

-Mawu a Mulungu amene ankaŵaphunzitsa Yesu ndi chimodzimodzi ndi Mawu a Mulungu amene ife tikukuphunzitsani tsopano.

-Mawu a Mulungu sasintha.
-Mawu a Mulungu ndi chimodzimodzi kwa anthu onse.

-Mulungu akufuna kuti mudzitimvera tikamakuphunzitsani Mawu a Mulungu ngati m’mane anthu ankamumverera Yesu pamene ankaŵaphunzitsa Mawu a Mulungu.

-Chifukwa chakuti Yesu ankaphunzitsira m’nyumba ndipo anthu ambiri ankabwera kudzamvera kuphunzitsa kwa Yesu, munalibe malo amene anatsala m’nyumbamo.

-Ngakhale kunja kwa chitseko kunalibe malo.
-Pamene Yesu ankaphunzitsa, anthu ena anabwera ndi munthu odwala manjenje.

Tiyeni tiŵerenge Maliko 2:3

3-Anthu ena anabwera kwa Iye, atatenga munthu odwala manjenje, amene ananyamulidwa ndi anthu anayi.

-Kodi munthu odwala manjenjeyo anakatha kudzichiza yekha?
-Iyayi.

-Kodi anzache a munthu odwala manjenje aja anakatha kumuchiza iye?
-Iyayi.

-Kodi sing'anga anakatha kumuchiza munthu wa manjenje uja?
-Iyayi.

-Palibe amene angathe kudzipulumutsa yekha ku mphamvu ya tchimo, imfa ndi Satana ngati m'mene ankalephelera munthu odwala manjenje uja kudzichiza yekha.

-Kodi anthu aja anachita chiyani ndi munthu odwala manjenje uja?

Tiyeni tiŵerenge Maliko2:4

4-Pakuti sanakatha kufika kwa Yesu ndi munthu odwala manjenje uja chifukwa cha khamu la anthu, anasasula denga pamene anali Iye, ndipo atatha kusasulapo, anatsitsa mphasa imene anagonapo munthu odwala manjenjeyo.



-Kodi ntchito ya  Levi inali yotani?
-Levi anali okhometsa msonkho.

-Levi ankaŵakhomela msonkho Aloma, kuchokera kwa anthu ache, Ayuda.

-Chifukwa chakuti okhometsa msonkho ankaŵakhometsa anthu a mtundu wawo, Ayuda, ndi kumapereka msonkhowo kwa Aloma, Ayuda sankaŵakonda.

-Ayuda sankaŵakondanso anthu okhometsa msonkho chifukwa chakuti iwo anali oyipa kwambiri.

-Anthu okhometsa msonkho ankaŵakakamiza Ayuda kulipira msonkho wambiri kuti ndalama zapambwazo zikhale zawo.

-Yesu anamuyitana Levi, okhometsa msonkho kuti amutsate Iye.

-Kodi chifukwa chiyani Yesu anamuyitana Levi okhometsa msonkho kuti amutsate Iye?
-Chifukwa chakuti Levi anamvetsetsa zakuti iye wamuchimwila Mulungu.

-Chifukwa chakuti Levi anamvetsetsa zakuti Mulungu amalanga machimo onse ndi imfa.

-Chifukwa chakuti Levi anamvetsetsa zakuti Mulungu yekha ndi amene angathe kumupulumutsa iye.

-Chifukwa chakuti Levi anamvetsetsa zakuti Yesu anali Mpulumutsi.

-Patapita zaka zambiri, Mulungu Mzimu Oyera anamutsogolera Levi kulemba limodzi mwa mabuku a Mulungu,

anamulemekeza Mulungu, ndikumati, “sitinaziwoneko zinthu ngati izi!”

-Yesu anaŵawuza anthu kuti Iye ali ndi udindo okhululukira machimo.

-Kodi chifukwa chiyani Yesu anali ndi udindo okhululukira machimo?
-Chifukwa chakuti Yesu ndi Mulungu.

-Yesu anawonetsa mphamvu zache ngati Mulungu weniweni pomuchiza munthu wodwala manjenje uja.

-Kodi chifukwa chiyani Yesu ankatha kuŵachiza anthu odwala?
-Chifukwa chakuti Yesu ndi Mulungu.

-Mulungu yekha ndi amene anakatha kuchiritsa munthu odwala manjenje uja.

-Pambuyo pache Yesu anapita ku mudzi wa Kapenamu umene unali pafupi ndi nyanja.

Tiyeni tiŵerenge Maliko 2:13-14

13-Kenako Yesu anaturukanso ndikupita m’mbali mwa nyanja. Ndipo linadza kwa Iye khamu lonse la anthu ndipo anayamba kuliphunzitsa.
14-Ndipo popita anawona Levi, mwana wa Alifeyu atakhala polandilira msonkho. Yesu anamuwuza kuti, “Nditsate,” nthaŵi yomweyo Levi anadzuka ndi kumutsata Iye.

-Pamene Yesu ankayenda, anakumana ndi munthu dzina lache Levi.



-Chifukwa chakuti panali anthu Ambiri amene ankamvera kuphunzitsa kwa Yesu, ndipo m’nyumbamo munalibe malo, anthu amene anamunyamula munthu odwala manjenje uja, anamutengera pa denga la nyumbayo.

-Anasasula denga la nyumbayo ndi kumutsitsila odwalayo pamene anasasulapo ali pa mphasa imene anagonapo mpaka patsogolo pa Yesu.

-Chifukwa chakuti Ayuda ankamanga nyumba zawo za madenga a udzu ndi matope ndipo ankakhala athyathyathya, anthuwo anatha kusasula dengalo ndi kumutsitsila munthu odwala manjenjeyo patsogolo pa Yesu.

-Kodi anthu aja anamupititsa kwa ndani munthu odwala manjenje uja?
-Kwa Yesu.

-Kodi ndi ndani yekha amene anakatha kumuchiza munthu odwala manjenje uja?
-Yesu.

-Kodi Yesu anachita chiyani?

Tiyeni tiŵerenge Maliko 2:5

5-Pamene Yesu anachiwona chikhulupiliro chawo, anati kwa munthu wa manjenje uja, “Mwana, machimo ako akhululukidwa.

-Yesu anawona kuti anthuwo akumukhulupilira Iye kwambiri, ndipo anamukhululukira munthu wodwala manjenjeyo machimo ache.

-Panali aphunzitsi ena a malamulo amene anali m’nyum-

bamo.

-Kodi aphunzitsi a malamulowo anaganiza chiyani pamene Yesu anamukhulullukira machimo munthu odwala manjenje uja?

Tiyeni tiŵerenge Maliko 2:6-7

6-Tsopano aphunzitsi ena a malamulo anakhalanso pomwepo akuganizira,
7-"Kodi chifukwa chiyani munthu ameneyu akulankhula chomcho? Akunyoza! Kodi amene angathe kukhululukira machimo ndi ndani, si Mulungu yekha?"

-Aphunzitsi a malamulo ankaganiza kuti Mulungu yekha ndi amene angathe kukhululukira tchimo.

-Kodi aphunzitsi a malamulowo ankaganiza bwino?
-Inde.

-Kodi ndizowona zakuti Mulungu yekha ndi amene angathe kukhululukira tchimo?
-Inde.

-Kodi wamsembe angathe kukhululukira tchimo?
-Iyayi.

-Koma chifukwa chakuti Yesu ndi Mulungu, Yesu akhoza kuŵakhululukira anthu machimo awo.

-Aphunzitsi a malamulo ankaganizanso kuti Yesu ankamunyoza Mulungu.

-Kodi aphunzitsi a malamulowo ankaganiza bwino?
-Iyayi.



-Kodi ndizowona zakuti Yesu ankamunyoza Mulungu?
-Iyayi.

-Yesu sankamunyoza Mulungu.

-Kodi Yesu ankadziŵa zimene aphunzitsi a malamulowo ankaganiza?

Tiyeni tiŵerenge Maliko 2:8

8-Nthaŵi yomweyo Yesu anadziŵa mu mtima mwache kuti akuganiza chomcho mwa iwo okha, ndipo analankhula nawo kuti, "Kodi chifukwa chiyani mukuganiza zinthu izi m'mitima mwanu?"

-Ngakhale kuti aphunzitsi a malamulo sanalankhule china chilichonse, Yesu ankadziŵa zimene ankaganiza.

-Chifukwa chakuti Yesu ndi Mulungu, ankaŵadziŵa maganizo a anthu onse.

-Kodi kenako Yesu analankhula chiyani?

Tiyeni tiŵerenge Maliko 2:9-12

9-[Yesu anati] "Kodi chapafupi ndi chiti: kunena kwa munthu wodwala manjenjeyu kuti, "Machimo ako akhululukidwa," kapena kunena kuti, "Dzuka, tenga mphasa yako ndipo uyende?"
10-koma muyenera kudziŵa kuti Mwana wa Munthu ali ndi udindo okhululuka machimo pa dziko la pansi pano…"
11-"Ine ndikukuwuza kuti, dzuka, ndipo tenga mphasa yako ndipo upite ku nyumba."
12-Anadzuka, natenga mphasa yache ndi kumapita pa maso pa anthu onse. Izi zinazizwitsa anthu onse ndipo